

Kulimbana ndi Vuto Losowa Ocheza Nawo



1

GANIZIRANI ZIMENE ZIMACHITITSA VUTOLO

Fotokozani nthawi imene mumaona kuti mukusowa anthu ocheza nawo.

.....

.....

Kodi zochita za anthu ena zikuwonjezera vuto lanu losowa anthu ocheza nawo? Ngati zili choncho, chikumachitika n'chiyani?

.....

.....

.....



2

DZIFUNSENI MAFUNSO MOONA MTIMA

Kodi ndi zinthu ziti zimene mwina *inuyo* mumachita zomwe zawonjezera vuto loti muzisowa ocheza nawo? (Mwachitsanzo: Kodi mumadziona kuti ndinu wosafunikira? Kodi nthawi zambiri mumakonda kuweruza ena kapena simuchedwa kukwiya?)

.....

.....

.....



3

CHITANIPO KANTHU (Agalatiya 6:5)

Mwina inuyo *si amene mwachititsa* kuti muzisowa anthu ocheza nawo, koma kodi mukuganiza kuti muli ndi *udindo* wotani pa nkhanayi?

.....

.....

Lembani mayina a *anthu* awiri omwe mungayesetse kuti mucheze nawo mlungu uno.

.....

.....

Lembani zinthu ziwiri zimene mungachite mlungu uno zomwe zingakuthandizeni kuti muthane ndi vuto losowa ocheza nawo.

.....

.....



4

GANIZIRANI ZOTSATIRA ZAKE

Kumapeto kwa mlungu uliwonse, onani ngati zinthu zikusintha. Kodi vuto lanu losowa ocheza nawo lachepa? Ngati silikuchepa, kodi mungachite zinthu zina ziti?

.....

.....

.....



Zimene zingakuthandizeni: “Ngati mumavutika kuti mupeze anthu ocheza nawo, choyamba yesetsani kukonza ubwenzi wanu ndi anzanu amene muli nawo panopa. Chachiwiri, pezani anzanu atsopano ndipo chachitatu, yambaninso kucheza ndi anzanu akale. Kulankhula ndi mnzanu amene munkacheza naye kalekale kungakuthandizeni kwambiri.”—Anne.

Kuti mudziwe zambiri, werengani pa Intaneti nkhanu yakuti “Zimene Achinyamata Amadzifunsa—N’chifukwa Chiyani Ndiliba Anzanga?” Pitani pa jw.org ndipo fufuzani pagawo lakuti **ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA > ACHINYAMATA.**